

# ZITSIMIKIZO ZOKHUDZA KUBWEZERETSA MIKANGO MU NKHALANGO

**Tikuzindikila** kuti mikango ili pa chiopsezo cha kutha munkhalango, ndipo mikango yambili yafa muzaka 25 zapita, kotelo kuti mu Africa muli chabe mikango 20 000. Mwaichi, tikuzipeleka kuthandiza mikango, nkhalango ndi anthu okhala kumalo komwe kupezeka mikango kukala ndi umoyo wabwino.

**Tikuzindikila** kuti atsogoleli amadziko ya mu Africa pamodzi ndi anthu onkhala kumalo komwe kupezeka mikango ndiwo atetezi eni eni a mikango mu Africa.

**Tikuzindikilanso** kuti mikango ndi chuma cha dziko iliyonse.

**Tikudziwa** kuti mikango ingathe kuchulukanso mu nkhalango zanthu ngati taiteteza bwino.

MWAICHO TIKUZIPELEKA PAKUTHANDIZA :

## KUTHESA KUTHA KWA MIKANGO

Tifunika kuteteza mikango, malo amene ikhalamo ndi nyama zimene mikango imadya.

## KUCHEPESA MABVUTO ANTHU AKUKUMANA NAO KAMBA KA MIKANGO

Tifunika kuchepesa mabvuto anthu akupeza kamba kakunkhala pafupi ndi mikango.

## KOSONYEZA PHINDU YENI-YENI YA MIKANGO KU ANTHU

Anthu onse afunika kuzindikila phindu ya mikango pa miyambo yathu, zachuma ndi kuzachilengedwe pa dziko.

